

LIU LA NAMIKANGO

Namikango Mission



Volume 1, 10 July 2014

Ndifuna Ndidze Yesu: Tanthauzo Lokhala Wophunzira Wa Yesu

Lemba la Wolemba:

Mwa chimwemwem ndi chiyamiko chachikulu tikulengeza za kuyambanso kutsindikiza Liu la Namikango. Ntchitoyi idayima kwa zaka zingapo chifukwa cha zopinga zingapo. Koma tayambanso kutsindikiza ntchitoyi kufikira nthawi yomwe Ambuye atikonzere kutsogoloku.

Palibe kusintha kwakukulu komwe kukhalepo mu nkhani za mu dongosolo lathu. Tipitiliza kuyika zidziwitso zina monga maliro, maulendo ndi zina zotero. Kusintha kowoneka komwe kulipo ndi kwa katumizidwe kake. Mosiyana ndi njira yomwe tidazolowera ya pa Positi, tidzatumiza mitokoma ya Liu la Namikango ku malo angapo komwe atsogoleri azikatengako ndi kugawa ku mipingo yomwe atumikirako.

Izi ziri dero pofuna kupulumutsa ndalama zambiri zomwe zinkangotayika chifukwa cha ma adiresi omwe adasiya kugwira ntchito ndipo mero inkangobwezedwa titalipira kale ndalama zambiri. Komanso njira imeneyi iwoneka yachangu, yosakayikitsa ndi yosawononga ndalama zambiri.

Titakambirana ndi kupemphera, tidavomerezana kuyamba ndi mutu womwe ukhale ukuyang'ana kwambiri 'Yesu Khristu.' monga nkhani yaikulu. Ndipo tagawa nkhanayi mu magawo awiri. Mu gawo loyamba tiphunzira moyo womwe udalimbikitsa Paulo mu chikhulupiriro chake, poyang'ana gawo la kalata yake yomwe adalembera kwa Afilipi. Tipitiriza kuwona moyo wa Paulo mpaka gawo lachiwiri.

Kenako tidzapitiriza monga mwa nthawi zonse. Chaka chino takonza kuti nkhani yaikulu ikhale yoyang'ana mozama kwa Khristu monga tsinde lenileni la chikhristu chathu.

Tikuthokoza nonse chifukwa chofuna kudziwa chifukwa chomwe tidayimira osalembanso Liu la Namikango. Izi zidathandiza kuti Mulungu alowererepo pomva mapemphero athu, ndikubweretsa kuthekera koti ntchitoyi iyambenso. Lero *Liu la Namikango* layambanso kumveka. Ambuye alemekezeke!

-Ben Hayes

Pofuna kuti awerengi athu amvetse bwino phunziroli, tatenga mau ambiri mu Chichewa cha lero chopezeka mu Buku loyera (*Copy right 1988 by The Bible Society of Malawi*).

Phil. 4:10-11

"I want to know Christ and the power of his resurrection and the fellowship of sharing in his sufferings, becoming like him in his death, and so, somehow, to attain to the resurrection from the dead."

See Announcements on page 8

Gawo 1: Ufulu Wake Wochoka Kuzilungamitsa

Pamene timva liwu lakuti *wophunzira*, nthawi zambiri mau omwe amabwera kumtima kwathu ndi a munthu yemwe ali mkati molandira maphunziro. Ophunzira amaphunzira kuchokera kwa mphunzitsi ndi cholinga choti tsiku lina adzakhoze kuphunzitsanso ena. Koma kukhala wophunzira kumapyola pamenepa. Wophunzira amafuna kuphunzira ndikupeza chidziwitso chomwe mphunzitsi wake ali nacho, komanso, kuwonjezera pamenepa, wophunzira amafunitsitsa atafanana ndi mphunzitsi wakeyo m'moyo ndi makhalidwe ake onse.

Mu nthawi ya Yesu kunali mau ena omwe anthu ambiri ankagwiritsa ntchito oti, “Kuyenda mu pfumbi la mphunzitsi wako.” Ayuda adali ndi aphunzitsi awo omwe ankawatchula kuti *Rabbi*. Rabbi adali aphunzitsi a malemba omwe adaphunzira mozama kwambiri. Rabbi ankatenga ophunzira omwe nawonso cholinga chawo chachikulu chidali kukhala ndi khalidwe longa la Rabbiyo. Kutanthauza kuti ophunzirawo, “Adayenda motsatira pfumbi la mphunzitsi wawoyo.” Wophunzirayo ankayenda motsatira pafupi kwambiri ndi mphunzitsi wakeyo kulikonse komwe ankapita, zomwe ankachita, kotero kuti pfumbi lonse lomwe linkafukulidwa ndi nsapato zake poyenda, linkathera mthupi la wophunzirayo.

Pamene ndimva nkhanu imeneyi, ndimaganizira za ubale wanga ndi Yesu. Kodi chidwi changa chikufanana ndi chimenechi choyenda pafupi naye, kotero kuti pfumbi la kumapazi kwake limandidzadza? Kodi timaonadi chithunzi chimenechi cholakalaka kufanana naye Yesu? Tikudziwa kuti ambiri a ophunzira a Yesu anali oti adzakomana ndi imfa kutsogolo kwa miyoyo yawo chifukwa chodzipereka ndi ku tumikira Yesu. Kodi nchiyani chomwe chingayambitse mwa munthu moyo wodzipereka chotere? Mu phunziro lathu titsatira khalidwe la mmodzi wa ophunzira a Yesu, Paulo.

Tiwona mau ake kwa Afilipi, makamaka mu mutu 3 ya kalata imeneyi kuti tiphunzire zinsinsi za kudzipereka kwake kwa Khristu.

Tiyeni poyamba tiwunike nkhanu mwachidule.

Mu machaputala angapo oyamba, Paulo akuthokoza Afilipi chifukwa cha kudzipereka kwawo kwa Khristu. Ndipo akuwalimbikitsa mmoyo wawo wotumikira, womwe tikuwona mu *Afilipi 4:15-17*, kuti ndi womwe udapangitsa Paulo kuwathokoza. Mu kalatayi, imodzi ya nkhanu zazikulu ndi chimwemwe kapena kukondwa. Chifukwa cha chimenechi, Paulo akupereka chenjezo mu chaputala 3 kuti asamale ndi anthu ena omwe angawalande chimwemwechi.

Mu *ndime 2* iye akuti, “*Chenjera nawoni ochita zaugalu aja, ndiye kuti ochita zoipa, anthu omangodula thupi chabe.*” Koma anthu amenewa kwenikweni ndi ndani? Anthu amenewa ndi Ayuda omwe akulimbikitsa anthu ena otembenuka

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

kuchokera kwa amitundu kuti adulidwe poyamba asadalandiridwe mgulu la otembenuka. Iwowa akulimbikitsa chiphunzitso chakuti kulowa mu ufumu wa kumwamba kumafuna kukhulupirira Yesu Khristu kuonjezera kanthu kena. Iwo ankati, “Inde muyenera kukhulupirira Yesu kuti mutembenuke. Komabe, muyeneranso kudulidwa.” Mu nthawi imeneyi chiphunzitso chimenechi chidali chisadafalikire pakati pa Afilipi. Paulo adangofuna kuwachenjezeratu. Pamenepa zikuoneka kuti anthu amenewa ankaganiza kuti kungokhulupirira Yesu kokha sikudali kokwanira ayi, kudasowekanso zina zowonjezera.

Mu kalata yake kwa *Agalatiya 1:6-7*, Paulo adatchula chiphunzitso chimenechi monga, “*Uthenga wabwino wina.*” Uthenga wonena kuti powonjezera pa kudziwa Yesu pamafunika zina, si uthenga woona ayi. Chiphunzitso chimenechi nchongotsutsana ndi Uthenga weniweni wabwino. Mu Uthenga wabwino, nkhani yonse imanena za Yesu yekha basi.

Mu Uthenga wabwino wa *Mateyu 7:15*, Yesu akutichenjezanso za anthu ena omwe amabwera monga nkhoa koma mkati ali Afisi olusa. Nthawi zambiri anthu amenewa sachokera kunjira kwa Mpingo ayi, iwo amakhala opembedza amene. Khalidwe lolimbikira kusunga malamulo a chipembedzo ndi limodzi mwa makhalidwe omwe akusautsa Mpingo kufikira masiku ano. Kumipingo yambiri masiku ano kulibe mtendere weniweni chifukwa cha khalidwe limeneli, lolimbikira ndi kutsamira pa malamulo ndi zikhulupiriro za chipembedzo.

Mu *ndime 3*, Paulo akupitiriza kuphunzitsa kuti, “*Paja ifeyo ndiye oumbala enieni.*”Kutanthauza kuti aliyense wovomereza ndi kukhulupirira Yesu Khristu kukhala Ambuye wake, amakhala mmodzi wa mu Ufumu wa Mulungu, kaya ndi wa mtundu wanji, fuko lanji, adalowa Mpingo liti, amasunga miyambo yanji. Onsewo amalandiridwa mu Ufumu wa Mulungu chifukwa cha ntchito yayikulu yomwe Yesu adayigwira, osati “kudalira miyambo ndi zizolowezi kapena zikhulupiriro za thupi.” Zoona zenizeni ndi zakuti anthu tonse timalowa mu Ufumu wa Mulungu mwa chisomo cha Yesu, mwa ulere, chifukwa cha ntchito yaikulu yomwe Iye yekha adayigwira, osati zomwe ine monga munthu ndingachite mwa thupi (*Aefeso 2:8*).

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

Tiyeni tsopano tifike pa nkhani yaikulu mu phunziro lathuli: *ndime 4 mpaka 14*.

Onani malembawa m’*mabibulo anu*.

Tonse tili ndi makhalidwe ena omwe timadziwika nawo, monganso momwe adaliri mtumwi Paulo, malingana ndi ndime 4 mpaka 6: “*Sindiyesanso pandekha kukhala wolungama,*” (*ndime 9*). Chilungamo kapena chiyero chomwe chikunenedwa pamenepa ndi chomwe timayikapo chikhulupiriro chathu; chinthu chomwe chimawonetsa kufunikira kwathu. Kwa Paulo, mndandanda wa zinthu zimenezi ndi womwe udali monga chilungamo chake. Kodi zinthu zimenezi ndi ziti?

Iye ndi Mhebri weniweni (mtundu wa munthu udali wofunikira kwambiri); Iye adali Mfarisi wodziwika bwino pakati pa Afarisi onse, adali wosunga ndi kusamala bwino malamulo a Mulungu. Iye sadachite zinthu zimenezi mwamasewera kapena mwachibwana ayi. Adachita zonse ndi mtima wonse pofuna kutsatira Mulungu, kotero kuti adalolera kuzunza Mpingo, poganiza kuti anthu onse omwe adali mu Mpingo ankapereka chiwopsezo ku ufumu wa Mulungu wake.

Pamenepa Paulo akufuna kunena kuti ngati pali wina yemwe adayesetsa kuchita bwino kapena kudziyeretsa mwa kuchita ntchito zabwino, adali iyeyo. Choncho ngati wina angafike pamaso pa Mulungu ndi kunena kuti, “Mulungu wanga taonani ntchito yomwe ndimachita, chonde ndilandireni chifukwa cha ntchito zangazi,” Paulo akadakhala mmodzi wa oterowo.

Mchitidwe umenewu ndi womwe udamufikitsa Paulo pomwe adafikapo. Zimenezi ndi zinthu zomwe iye adazikhulupirira. Ngati munthu utsamira khoma ndi mphamvu zako zonse, khomalo likagwa, iwenso udzagwa nalo pamodzi. Monganso Paulo, tonse timakhala nazo zinthu zina zomwe timazona monga “zotiyeretsa ndi kutilungamitsa.” Ngati tiyika chikhulupiriro chathu mu zinthu zotiyeretsa ndi kutilungamitsa tokha, zitanthauza kuti moyo wathu wonse watsamira pa zimenezo. Kodi zinthu zimenezi zingakhale monga chiyani kwa ine ndi inu?

Mwina ndimalandira ulemu wowirikiza kuchokera kwa anthu. Mwina ndiri pa ntchito yabwino yomwe imandipatsa malipiro a pamwamba. Mwina ndine wophunzira kwambiri. Kapena anthu amanditenga monga mtsogoleri wodzadzidwa ndi chiphunzitso chokwanira bwino pa Mpingoponse. Mwina anthu amanditenga monga mtsogoleri wodzala ndi Mzimu.

Zimenezi ndi zinthu zina zomwe timakhulupirira zimawonetsa kufunikira kwathu ku magulu komwe tikhala. Timakhulupirira kuti zimatithandiza kuti anthu, mosazindikira, atilandire ndi kutiyamikira motipatsa ulemu monga anthu a phindu. Koma tayambani mwakhala chete, ndikuganizira zinthu zimenezo zitalandidwa kwa inu. Kodi pamene panso kudziwa Yesu kungakhale ndi phindu? Kodi mungathe kuvomerezabe kuti Mulungu akukulandiranibe ndi kukukondanibe, makamaka tsopano pamene mulibenso zomwe munkazidalirazo?

Kodi pamene Paulo akutiphunzitsa chiyani pa zinthu zomwe iye ankadziwika nazo? Mu *ndime 7*, Iye akuti, “*Ndikuziona kuti nzosapindula.*” Kutanthauza kuti nyansi, zitosi kapena ndowe. Zonse zomwe anthu ambiri amazitenga monga zinthu za phindu, Paulo akuti kwa iye ziri monga nyansi. Koma nchiyani chidampangitsa Paulo kufika ponena mau onga amenewa? Mosakayika, Paulo adapeza chinthu china cha mtengo wa patali.

Kodi chinthu chimenechi nchiyani?

Yesu Khristu!

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

“Inde,” tikhoza kutero. Tikudziwa kuti ndi Yesu. Koma ndikupemphani kuti timvetse bwino nkhanayi. Paulo wapeza, kapena kuti watulukira chinsinsi chomwe chasintha moyo wake wonse

kotheratu. Tiyeni tsono tikhale nayo nthawi yomvetsera bwino chomwe akutanthauza chifukwa nkhanayi ndi yofunikira kwambiri kwa ife tonse.

Poyamba, mau oti, “*Ndikuziona kuti nzosapindula,*” akutanthauza kuti ngakhale Paulo adali ndi zinthu zomwe ankazitenga monga zofunikira ndi zomupatsa ulemu, iye tsopano wawona kuti Yesu apambana zonsezo. Kaya zidali zapindu lotani, phindu lakelo ndi laling’ono kwambiri pofanizira ndi phindu lopezeka mwa Yesu. Ziri monga momwe dzuwa.

Pamene lituluka mmawa, kuwala ndi kuthwanima kwamphamvu kwa nyenyezi sikuwonekansa. Izi ziri chomwechi chifukwa mphamvu za kuwala kwa dzuwa zimaposa kuwala kwa nyenyezi. Paulo adali munthu mmodzi wolemekezeka kwambiri pakati pa Ayuda. Izi zidali chomwechi malinga ndi mndandanda wa zoyenereza zomwe wafotokozazi. Koma pamene adasankha kusiya chiyuda ndikuyamba kutsata Khristu, Ayuda sadamulemekezansa.

M’mawu omveka bwino, tikunena kuti Paulo adalolera kutaya ulemu ndi mphamvu zake zonse pakati pa abale ake chifukwa chosankha kukhala mkhristu.

Malinga ndi kufotokoza kwake mu chaputala cha m’buyomu cha 2, iye wapereka chithunzithunzi cha Yesu akuwonetsa khalidwe longa limeneli. Ngakhale Yesu adali Mulungu, Iye sadafune kukakamira Umulungu wakewo ayi, Iye adataya ulemu wonsewo chifukwa cha anthu. Choncho Paulo, nayenso akuyenda mmapazi a Yesu, potaya zonse zowoneka monga zofunikira pa moyo ndi ulemu wake.

Zimenezi nzothekansa ngakhale kwa ife, tikhoza kusiya zonse zowoneka monga zotipatsa ulemu ndi mphamvu, maka podziwa kuti Yesu adakhoza kale kuchita zomwezo. Yesu satilangiza kuchita zinthu zomwe Iye sadachitepo ayi.

Tisayiwalenso kuti mphoto zimayambira pansi pomwepano. Pamene Paulo akunena kuti, *“Ndikhoza kuchita zimenezi mmoyo wanga wa nthawi ya pansi pano; ndidzatayikitsa zonsezo, chifukwa tsiku lina ndidzalandira mfupo,”* akufotokoza za moyo wa lero, kumudziwa Yesu lero. Ndipo kudziwa Yesu nthawi ino ndi chinthu chokondweretsa zedi, chinthu chokwaniritsa ndi kudzadzitsira moyo wanga wa Uzimu kuposa nkhani ina iriyonse pa dziko lapansi.

Kachiwiri, ngakhale Paulo akunena kuti, *“Ndikuziona kuti nzosapindula,”* akutanhouza kuti ayenera kuzitenga monga zopanda pake ngati iye akufuna kudziwa Yesu. Ngati kudziwa Yesu chidali cholinga chake chachikulu, sakadataya nthawi yake pokangamira ndi kutanganidwa ndi zinthu zimenezi. Kukadakhala kovuta, chifukwa sikukadatheka kusunga ungwiro wake pamodzi ndi wa Yesu. Kodi pamenepa chikutanhouza chiyani? Ngati zinthu zomwe timazikangamira monga zofunika kwambiri, monga zotilungamitsa zathu, tiziyika mmoyo wathu monga zofunikira kwambiri, sitingathe kudziwa Yesu mokwanira bwino.

Chifukwa chiyani? Tikuzitenga zinthuzo monga zapamtima pathu penipeni, koma Yesu wanenetsa kuti Iye sagawana malo ndi zina kapena china chirichonse cha thupi. Nthawi yomwe ife timapeza mtendere ndi chimwemwe chenicheni ndi nthawi yomwe Yesu walowa ndi kutenga malo ofunikira mumtima mwanga, omwe ndinkayikamo zinthu zina za thupi zomwe zinkanditangwanitsa kale. Okondedwa, Yesu sindidzamufikira chifukwa cha ubwino, kudziyeretsa kapena kuchita bwino kwanga, ayi.

Nkoyenera kutaya ndi kuyiwala zanga zonse. Yesu timamufikira chifukwa cha chisomo chake basi, apo ayi, nkosatheka. Tiyenera kutaya zonse zodziyeretsa kapena kuzilungamitsa nazo. Chisomo, monganso lamulo liri, nachonso chiri ndi zoyenereza zake. Kuti kutheke kwa munthu kulandira chisomo chomwe chingagwire ntchito kwa iyeyo, munthuyo ayenera kudziwa ndi kuvomera kuti iyeyo ndiwolephera, wosayenera kulandira chisomocho, ndipo kuti palibe ntchito ina iriyonse yabwino

yomwe mudachita, mungachite, kapena mumachita yokuyenerezani kulandira chisomo chimenechi. Choncho monga Paulo mtumwi, tiyeni titaye zonse zomwe timazona monga zoyenera kuzikangamira chifukwa chakufunikira kwake.

Kuchokera pamenepa ndi pomwe timapeza chimwemwe chopambana. Izi zimatero chifukwa Khristu amalowa ndikutenga malo onse momwe mudali zonse zotitangwanitsa monga zofunikira kwa pa moyo wathu. Tisamakhale ndi maganizo oti kudziyeretsa kwathu kwa ife eni ndi komwe kungatifikitse kwa Yesu ayi.

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

Tiyenera kutaya zonsezo. Dziwani kuti muyenera kuyanjanitsidwa ndi Khristu kudzera mu chisomo chake chokha basi, zina zonsezo ayi nkosatheka. Chisomo, monga momwe lirili lamulo, nachonso chili ndi zoyenereza zake. Kuti chisomo chigwire ntchito yake, chilandirike pa munthu, munthuyo ayenera kumvetsa ndi kuzindikira kuti iye sali woyenera ndiponso palibe ntchito ina iriyonse yabwino yomwe angachite yoposa imfa ya Yesu yomwe munthu angachite kuti ikamyandikitse kwa Mulungu. Choncho monga Paulo, tiyeni titaye zonse zomwe zimatenga malo a Yesu mu mitima yathu.

Nkhaniyi ndi yofunikira kwambiri. Tiyeni tiphunziremo zinthu zingapo. Mndandanda wa zinthu zomwe Paulo wafotokoza muli zabwino zokhazokha. Zinthuzi simachimo omulepheretsa kuyanjana ndi Khristu. Mu njira ina, Paulo akufotokoza kuti zinthuzi sizinthu zoti ayenera kuyamba wazisiya asadayanjane ndi Khristu. Komabe ayenera kuthana nazo kuti kudziwana kwake ndi Khristu kusavute.

Kwa ife monga Akhristu, nthawi zambiri timaona ngati ‘machimo’ athu ndi omwe amatisiya kutali ndi Mulungu. Komatunso dziwani kuti nthawi zambiri kulungama kwathu ndi komwe kumatilekanitsa ndi Mulungu. Ndikudziwa kuti nkhani imeneyi ndiyovuta kumvetsa bwino, choncho chifukwa cha chimenechi, nkhani imeneyi ndi yowopsa kwambiri kuposanso uchimo wodziwikiratu uja.

Mwina sitikuzindikira kuti zimenezi zingakhale zikuchitika. Mu *chaputala 7 cha buku la Luka* tikuwona Mfarisi mwini nyumba, komwe Yesu adali ndi ophunzira ake akuyipidwa ndi mai wachiwerewere yemwe ankatsuka mapazi a Yesu ndi misonzi yake, nawatsira mafuta onunkhira. Iye adafunsa kuti, “Kodi simudziwa kuti ameneyu ndi yani?” Ndipo Yesu adamuyankha kuti mayi uja ndi yemwe adali ndi chikondi choposa chifukwa mayiyo ankalakalaka atalandira chikondicho.

Mayi uja adatha kuwona, kuzindikira ndi kuvomereza tchimo lake, choteronso anali wokonzeka kulandira chikhululukiro cha Yesu ndi chimwemwe chonse. Iye adazitenga monga wosayenera kulandira chikhululukirocho. Koma anthu omwe satha kuwona, kuzindikira ndi kuvomereza tchimo lawo sangathe kulandira chikhululukiro ndi chisomo, chifukwa satha kuwona vuto lawo. Iwo amawona ngati ndi woyera kale, zawo ziri bwino.

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

Kumeneku ndiko kuwopsa kwa zotsatira zoganizira kwambiri za ungwiro wanga, zodziyeretsa ndekha. Moyo wodziyeretsa tokha umatisiya kutali ndi Mulungu chifukwa timaganiza kuti zonse ziri bwino. Komanso timaganiza kuti ngati pali wina wolephera, ndi ena, osati ife ayi. Koma dziwani kuti Yesu adabwerera odwala; Yesu adabwerera okhawo omwe

akumusowadi; onse omwe ali osauka mu mzimu (*Mateyu 5:3*).

Poyambira pabwino podziwana ndi Yesu padzikhala poti tidzizindikira za kufunikira kwake mu moyo wathu ndi kumfunsa kutichotsera zonse zotitangwanitsa zazikulu ndi zazing’ono zomwe, zodziwika ndi zosadziwika, pamodzi ndi moyo wodziyeretsa ndi kudziyesa angwiro mwa ife tokha. Iyi ndiyo njira yabwino yomwe imatithandiza kupezeka tiri mwa Yesu, monga mwa mau a Paulo pa *ndime 9*, akuti, “*Ndi kupezedwa mwa Khristu.*”

Dzina latsopano lomwe tiri naloli silidabwere chifukwa cha kuthekera kwathu ayi, koma ndi chifukwa chakuti timamvetsa ndi kuvomereza kulira kwa mtima wathu chifukwa chosowa Yesu. Palibenso china choposera chimenechi pa dziko lapansi lonse. Ndi nkhani yopatsa chidwi kwambiri. Taganizani, kulandiridwa ndi kukondedwa chifukwa eti, chongovomereza kuti indedi, ine ndikukusowani. Ndizopatsadi chidwi chifukwa pamenepa zikutanthauza kuti aliyense yemwe apezeka ‘mwa Khristu’ ali ndi mwawi wolowa nawo mu chisangalalo chimenechi. Zinthu zimakoma nkugawana.

Tsopano tonse tidziwika monga amodzi. Kulibenso kudziwika ndi chiwongo, mtundu, mbiri ya banja lathu, mwamuna kapena mkazi, maphunziro, kulemera kapena kusauka, kuphunzira kapena kusaphunzira, chiphunzitsa chomwe ndidziwa ndi zina zotero. Mulungu akamatiyang’ana, amatiwona monga momwe awoneranso Yesu. Abale, zimenezitu ndi zosangalatsa!

Inde, taona zinthu zambiri, koma cholinga chenicheni chinali chofuna kuphunzira tanthauzo la kudziwa Yesu. Tsono tafika pa phata penipeni pa nkhani yathu. Koma tisadapitirire, tiyeni tikhalenso ndi kanthawi kowonanso zomwe taphunzira. Tonse timadzipereka kwa Yesu koma tiri ndi katundu winanso yemwe amakhala ndi gawo la momwe timdziwira Yesuyo.

Katundu ameneyu amakhoza kukhala monga mavuto omwe takomana nawo m'mbuyomo, moyo wathu wa Uzimu, miyambo, makhalidwe ndi zizolowezi zathu zina ndi zina zotero. Choncho chifukwa cha zimenezi, tonse timalephera kukhala ndi chithunzithunzi chowoneka bwino cha Yesu.

Pamenepa tikuona kuti kuphunzira kumudziwa bwino Yesu ndi kukhala ndi chithunzithunzi chake chowoneka bwino ndi ntchito yomwe imatenga kanthawi, maka chifukwa cha katundu yemwe amatseka maso athu kuti awone bwino. Tidzamdziwa Yesu pamene pang'onopang'ono tidzachatse akatundu otitseka mmaso aja.

Tsono kaya ndinu ongoyamba kumene ulendo wodziwa Yesu, kapena muli cha pakatikati pa ulendowu kaya ndi inu achiyamba kale, tawonani mafunso otsatirawa kuti akusiyani pati pa ubale wanu ndi Yesu:

1. Kodi ziripo nthawi zina zomwe mumaganiza kuti chipulumutso chanu chimadalira ntchito zomwe mumachita kwa Mulungu? Kodi maganizo amenewa amakufikirani chifukwa chiyani?
2. Kodi mumakhala nazo nthawi zomaganiza kuti ndinu woyenera kulandira chisomo cha Mulungu? Mukuganiza nchiyani chimakupatsani maganizo amenewa?
3. Kodi mau akuti, "*Chimwemwe*" amakufikirani mumtima mwanu pamene muganiza za ubale wanu ndi Khristu? Ngati sichoncho, bwanji, palibe chinthu china chake chokhudzana ndi momwe mumvera za kumasulidwa kwanu mwa Yesu, chomwe chimakuchotserani chimwemwe chanucho?
4. Kodi mungafotokoze bwanji kusiyana kwa pakati pa makhalidwe abwino ndi moyo wa

uzimu kwa munthu yemwe amaganiza kuti kungokhala ndi makhalidwe abwino munthu umalandiridwa ndi Mulungu?

5. Kodi mumamva kutsutsika ndi kupanda chiyembekezo mumtima mwanu pa ubale wanu ndi Mulungu? Kodi zimenezi mwina zikutanthauzanji pa momwe mudziwira za kulandiridwa kwanu ndi Iye?
6. Kodi ndi choona chiti chomwe chakupatsani chidwi lero mutawerenga Afilipi 3:3-9?

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

sdlfkjsdflkj
lsdjfslfdj

- sdlfjds
- lsdflkjdsf
-

“Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Condinmentum. Nullam Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet. Lorem Ipsum Dolor Set Ahmet In Wisi Acru Suscpit Consectetuer viviamus.”

Leo Praesen

Fusce ac leo

Purus, in consectetuer Proin in sapien. Fusce urna magna, neque eget lacus. Maecenas felis nunc, aliquam ac, consequat vitae, feugiat at, blandit vitae, euismod vel.

